


KUKHALA MOYO, KUFA, KUIKIDWA MMANDA, KUWUKA, AKUBWERA

 Izo ndi zoposa basi chirichonse chimene ife tingachifotokoze mu zinenero za umunthu, za mmene mitima yathu ikumverera, lero, pamene ife tasonkhana pano mmawa waulemu, wopatulika uno. Mmawa uno ukuimirira nthawi imene chipembedzo chathu chinapangidwa kukhala chenicheni, chifukwa kunali kuukanso kwa Mwana Wanu wofunika Amene anabwera kuti adzawombole mtundu wonse wa anthu. Ndipo ife tiri pano mmawa uno kudzakondwerera, kugonjetsa kwakukulu, kwapamwamba uko, Ambuye, kumene kunatipanga ife kukhala oposa agonjetsi a zonsezo imfa, gehena ndi manda. Ndipo ife tikukuthokozani Inu kuti, zitadutsa zaka zonsezi, ife tikumasonkhanabe molawirira mmawa pa mmawa wa Isitara uwu, kuti tidzamupembedze Iye, chifukwa ife tikukhulupirira kuti Iye akubweranso.

² Ndipo ife tikupemphera kuti Inu mukhululukire machimo athu onse ndi mphulupulu zathu zimene zalembedwa motitsutsa ife, pamene ife modzichepetsa tikuvomereza zolakwa zathu, ndi kuvomereza chitetezero Chake cha machimo athu. Chiritsani matenda amene ali pakati pathu, Ambuye. Mutithandize ife pamene tiziwerenga Mawu Anu Oyera, amene ali maziko a Choonadi chonse chimene Inu mwatisiira ife kuti tidzikhallira nacho moyo ndi kuchikhulupirira.

³ Ndipo ife sitikungopempherera gulu ili lokha limene lasonkhana pano, koma onse kuzungulira dziko, pakuti ife tikuyang'anira ndi maso achidwi ndi mitima yachiyembekezo kubwera Kwake. Ife taima lero mu mdima, mu chisokonezo, kuti pamene, pafupifupi nthawi iliyonse, kuti wotengeka wina akhoza kungophulitsa chinachake, ndi kuyatsa batani laling'onolo, ndipo dziko lonse likhoza kuphulitsidwa mu zidutswa. Monga zinanenedwa kwa ife ndi a maulamuliro aakulu, kuti, nkhoodoyo idzangokhala yotalika ma ora pang'ono, ngati iyo ingati idzachitikenso. Oh! Pamene, ife taima lero mmphepete kumene mwa nkhoodo ina. Pamenepo, Mpingo waima mmphepete, mwa chiukitsiro cha ulemelero waukulu icho, pakuti ife tidzatengedwera mmwamba limodzi ndi oyera amene akugona, kukakumana ndi Ambuye mu mlengalenga, ndipo kwanthawizonse kukakhala ndi Iye.

⁴ Ife tabwera kuti tidzakupembedzeni Inu, Ambuye. Ndipo tilandireni ife lero. Mudalitse kuwerenga kwa Mawu Anu, kuimba kwa nyimbo, kulalikira kwa Uthenga, mulandire mapemphero a olapa. Mumvere pemphero la odwala, ndipo mudzitengere ulemelero kwa Inumwini, pakuti ife modzichepetsa tikupempha izi mu Dzina la Yesu, Mwana Wanu. Amen.

⁵ Kwa inu amene mukufuna kuti mutenge pamene ife titi tiwerenge mmawa uno, kwa Malemba athu . . .

⁶ Ndipo ife tikupepesa kuti—kudziwa kuti ife tiribe malo okhalapo kwa gulu labwino ili la anthu amene abwera molawirira mmawa uno kuti adzapembedze limodzi ndi ife, kuchokera ku matchalitchi osiyanasiyana ndi madera osiyanasiyana, ndipo ngakhale ku mafuko osiyanasiyana, asonkhana mmawa uno pano pa Kachisi, pa kupembedza kwa ulemelero waukulu uku kwa Ambuye.

⁷ Ine ndikufuna kuti inu mutsegule ku Bukhu la Masalmo, Masalmo 22. Ine ndikudziwa kuti awa makamaka ndi malo osazolowereka kuwawerenga, kwa msonkhano wa Isitara, koma Mulungu ndi wosazolowereka.

⁸ Ndipo tsopano ukatha msonkhano uno, ife tiimikira kaye kwa pafupifupi ora limodzi, kuti inu muthe kupita ku kadzutsa wanu. Ndipo kenako msonkhano wa Sande sukulu udzayamba hafu-naini. Ndipo kenako ukangotha msonkhano wa Lamlungu, padzakhala msonkhano wa ubatizo kuno pa—dziwe. Ndiyeno madzulo ano, sikisi koloko, makadi a pemphero akhala akuperekedwa kwa msonkhano wa machiritso, wa usikuuno. Ndipo ngati inu muli nawo okonedwa aliwonse amene akudwala ndi osowa, mukumbukire kuwabweretsa iwo usikuuno, ndipo, pakuti iyi idzakhala nthawi yomaliza imene ife tidzakhale ndi uwu kwa—kanthawi, mulimonse. Ine ndizinyamuka mmawa, faifi koloko, kupita ku Los Angeles ndi kudutsa ku Gombe la Kumadzulo, ku mndandanda wa misonkhano.

⁹ Tsopano mu Masalmo 22, ife tikuwerenga.

Mulungu wanga, Mulungu wanga, nchifukwa chiyani inu mwandisiya ine? nchifukwa chiyani inu muli kutali kuti mundithandize ine, . . . ku mawu a kubuula kwanga?

. . . Mulungu wanga, ine ndimafuula masana, koma inu osandimva ayi; ndi mu nyengo ya usiku, ndipo ine sindiri chete.

Koma inu ndi woyera, O inu amene mumakhala mmatamando a Israeli.

Makolo athu anakudalirani inu: iwo anakudalirani ndipo inu munawapulumsa iwo.

Iwo analilira kwa inu, ndipo anapulumsidwa: iwo anadalira mwa inu, ndipo iwo sanakhumudwe.

Koma ine ndi nyongolosi, ndipo osati munthu; chitonzochanthu, . . .wonyozedwa ndi anthu.

Onse amene andiwona ine akundiseka monyozochitonzochanthu: iwo akupotoza mlomo, ndipo iwo akumagwedeza mutu, ndikuti,

Iye amadalira pa AMBUYE kuti amupulumutsa iye: siyani amupulumutse iye, powona kuti iye amasangalala mwa iye.

Koma inu ndi iye amene munanditenga ine kuchokera mmimba: inu munandipanga ine kukhala ndi chidaliro pamene ine ndinali pamabele a amayi anga.

Ine ndinaponyedwa kwa inu kuchokera mmimba: inu ndi Mulungu wanga kuchokera mmimba mwa amayi anga.

Musakhale kutali ndi ine; pakuti mavuto ali pafupi; pakuti palibepo aliyense woti andithandize.

Ng'ombe zamphongo zambiri zandizungulira ine: ng'ombe zamphongo zamphamvu zaku Basani zakhala mondizungulira ine.

Izo zandiyasamulira ine ndi kamwa zawo, ngati wolusa ndi . . .mkango wobuula.

Ine ndathiridwa ngati madzi, . . .mafupa anga onse aguluka: mtima wanga uli ngati mafuta; iwo asungunuka pakati pa matumbo anga.

Mphamvu zanga zauma ngati phale; . . .lirime langa lamatirira ku msagwada zanga: ndipo inu mwandibweretsa ine ku fumbi la dziko.

Pakuti agaru andizungulira ine: misonkhano ya oyipa yanditsekereza ine: iwo apyoza manja anga ndi mapazi anga.

Ine ndikhoza kuwerenga mafupa anga onse: kuti iwo akuyang'ana ndipo akuchita chidwi pa ine.

Iwo agawana zovala zanga pakati pawo, . . .apangira maere chovala changa.

. . .inu musakhale kutali ndi ine, O AMBUYE: . . .mphamvu zanga, inu mufulumire kundithandiza ine.

Pulumutsani moyo wanga ku lupanga; wokonedwa wanga ku mphamvu ya garu.

Ndipulumutseni ine ku kamwa la mkango: pakuti inu mwandimva ine kuchokera ku nyanga ya njati.

Ine ndidzatchula dzina lanu kwa abale anga: pakati pa onsonkhana ine ndidzakutamandani inu.

Eya . . . Inu amene mumawopa AMBUYE, mutamandeni iye; inu nonse mbewu za Yakobo, mulemekezeni iye; ndipo muopeni iye, nonse inu mbewu za Israeli.

Pakuti iye sananyoze kapena kudana ndi mazunzo . . . iye sanabise nkhope yake kwa iye; koma pamene iye analilira kwa iye, iye anamva.

Kupembedza kwanga kudzakhala kwa inu kwa osonkhana ochuluka: ine ndidzapereka malumbiriro anga pamaso pa iwo amene amamuopa iye.

Ofatsa adzadya ndipo adzakhutitsidwa: iwo adzakupembedza AMBUYE amene akumufuna iye: mtima wanu udzakhala moyo kwa nthawizonse.

Mathero onse a dziko adzakumbukira ndipo adzatembukira kwa AMBUYE: ndipo mitundu yonse ya mafuko idzapembedza pamaso pake.

Pakuti ufumu ndi wa AMBUYE: ndipo iye ndi kazembe pakati pa mafuko.

Onse amene ali onenepa pa dziko lapansi adzadya ndi kupembedza: iwo onse amene apita pansu ku fumbi adzagwada pamaso pa iye: ndipo palibe amene angasunge solo yake ndi moyo.

Mbewu idzamatumikira iye; iyo idzawerengeredwa kwa Ambuye kwa m'badwo.

Iwo adzabwera, ndipo adzanenera chiyero chake kwa anthu ndipo adza . . . amene adzabadwe, kuti iye wapanga ichi.

¹⁰ Ambuye awonjezere madalitso Ake ku kuwerenga kwa Mawu Ake. Ine ndikufuna kuti nditenge pa chochitika ichi mmawa uno, mawu asanu, ndipo pozungulira mawu asanu amenewo ndiyesera kufotokoza chimene chiri pa mtima panga, kwa inu opembedza mmawa uno. Ine ndikufuna mawu asanu awa: *Kukhala Moyo, Kufa, Kuikidwa Mmanda, Kuwuka, Akubwera.*

¹¹ Ndipo ine ndikuganiza kuti wandakatulo anazifotokoza izo bwino mu nyimbo, za chimene ine ndikufuna kuti ndinene, pamene iye analemba nyimbo iyi.

Pokhala moyo, Iye anandikonda ine. Pakufa,
Iye anandipulumutsa ine.

Poikidwa mmanda, Iye anatengera machimo
anga kutali.

Powuka, Iye anandilungamitsa mwaulele
kwanthawizonse.

Tsiku lina Iye akubwera, oh, tsiku
laulemerero!

¹² Sipanakhalepo moyo umene unakhalidwapo wonga wa Iye, chifukwa Iye anali Mulungu akuwonetseredwa mu thupi pamene Iye anabadwa. Iye anali kuwonetsera kwa chimene Mulungu Atate ali. Ndipo Mulungu Atate pokhala chikondi, ndiye Yesu anali kuwonetsera kwamphumphu kwa chikondi. Iye anali chikondi kuchokera pa nthawi yoyamba imene manja Ake akhanda anamenya masaya okongola a amayi Ake. Iye anali chikondi.

¹³ Ndipo ine ndikuganiza lero kuti apo ndi pamene ambiri akulephera kuzindikira kuti Iye anali chikondi. “Mulungu ndi chikondi, ndipo iwo amene amakonda ndi obadwa mwa Mulungu.”

¹⁴ “Mulungu analikonda kwambiri dziko, amenewo ndi, osakonedwawo, mpaka Iye anampereka Mwana Wake wokonedwa yekhayo, kuti aliyense amene akhulupirira mwa Iye asawonongeke, koma akhale nawo Moyo Wosatha.”

¹⁵ Iye anawonetsera chikondi Chake pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, mu njira zambiri zosiyanasiyana, mpaka izo ndizosatsutsika kuti Iye anali cholengedwa chokonda kwambiri chimene chinayamba chakhalapo moyo. Ndipo ine ndikuganiza, nthawi ya moyo Wake kuno, Iye anali kumufotokoza Mulungu. Ndipo njira yokhayo imene Mulungu angathe kufotokozedwera kwa anthu ndi kudzera mu chikondi.

¹⁶ Ndipo Iye anachita izi mwabwino pamene Iye anakumana ndi mmodzi wa azimayi oyipitsitsa amene analipo a tsiku Lake, mwinamwake. Iwo anamupeza iye wolakwa basi, ndipo panalibe njira yoti apulumukirepo, pamene iye anapezeka ali mu chigololo. Ndipo iwo anamududuluzira iye kwa Iye, ndipo anati, “Kodi Inu mukuti tipange naye chiyani iye?”

¹⁷ Ndipo pamene Iye anapotokera kwa iye, ndipo, anati, “Ine sindikukuweruza iwe. Pita ndipo usakachimwenso.” Mmalo momuponyera iye ku misewu, kuti akamukhwekhweletse ngati gulu la ankhandwe pa iye, kuti akamugende iye ndi kuchotsapo moyo wake; mtima Wake wanthete, wachifundo, wachikondi unatsikira pansu mu tchimo limene iye anali alimo, anati, “Ine sindikukuweruza iwe. Ingopita ndipo usakachimwenso.”

¹⁸ Ndipo pamene Iye anali panjira Yake akutsikira kumanda a Lazaro, ine ndikuganiza kuti imeneyo inali nthawi ina yopambana imene Iye anafotokoza chimene Mulungu ali kwa anthu. Iye si Mulungu yekha amene angakhululukire tchimo lotsikitsitsa limene lingapangidwe, ndi kuwachotsera zolakwa ndi kuwapanga iwo kukhala osalakwa, mwa chikondi Chake chokhulukira, koma imfa itatha kutiika ife kuli chete, Iye amakhala wokhudzidwabe za ife. Ine ndikuganiza Iye anafotokoza bwino zimenezo panjira ali ndi Marita ndi Mariya, pamene Iye anadzafika kunyumba kumene imfa inali itachotsa moyo wa munthu wokonedwa. Ndipo ali panjira

Yake waku manda, komabe, pokhala Mulungu, ankadziwa kuti Iye akanadzamuukitsa iye kwa akufa, ankadziwa kuti zinanenedwa kwa Iye kuti mu Mawu Ake omwe munali Mphamvu yomuukitsa iye kuchokera mmanda; komabe, pamene Iye anawona Marita ndi Mariya ndi iwo amene ankamukonda Lazaro, akulira, Baibulo limati Iye analira. Chinali chiyani chimenecho? Mtima Wake wopambana wachikondi! Pamene Iye anamuwona mwamuna ameneyo, ndipo Ake—abwenzi Ake ali pamavuto, Iye anavutika nawo iwo.

¹⁹ Ndine wokondwa kwambiri kudziwa kuti Iye akhoza kupezeka pakati pa oswekamtima. Mu zisoni zathu, Iye si wina amene angatisiye ife. Iye amaima pafupi nafe pamene zonse zalephera, ndipo ziyembekezo zomaliza za mdziko zafika ku mapeto ake, iye amakhalabe Mulungu ndipo Iye amatikonda ife. Iye anali kufotokozera kwa Mulungu.

²⁰ Ndipo, oh, mmene ine ndimakhulupirira kuti Iye amafuna kuti anthu Ake akhale odzodzedwa kwambiri ndi Mzimu Wake, kuti ife tidzitha kumapita kwa wina ndi mzake mmayesero ndi mmavuto, ndi kukapereka kuwonetsera kwa chisoni Chake, pamene icho chikukhuthuka kuchokera mmitima yathu imene yabadwa mwa Mzimu Wake, kuti tizinyezimiritsa mu mpingo chikondi cha Mulungu wamoyo. Zimenezo zinafotokoza bwino zimene Iye ananena, kapena wandakatulo ananena.

Pokhala moyo, Iye anandikonda ine.

²¹ Iye anawonetsera chimene Iye anachita kwa mtundu wonse wa munthu, mmene Mulungu anadziimirira Yekha mwa Yesu Khristu. Iye anafotokoza maganizo Ake kwa mtundu wa munthu, kuti azikhululukira ndi kuwakonda iwo amene ali osakonedwa. Ndipo ine ndikudabwa, mmawa uno wa Isitara, mmene ife tikupezekera operewera pa zimenezo. Ife timakhoza kuwakonda iwo amene amatikonda ife, koma Iye ankawakonda iwo amene sankamukonda Iye.

²² Iye anali chachikulu kwambiri, choimirira choyamba, cha chikondi chimene chinayamba chagundapo pa dziko lapansi; ndipo ananyozedwa ndi iwo amene ankakhala pa dziko lapansi, iwo amene Iye ankawakonda. Palibe munthu amene ankakonda monga Iye; ndipo palibe munthu amene anadedwapo monga Iye. Iwo ankamuda Iye ndi kumunyoza Iye, ndi kumukana Iye, koma izo sizinaletse chikondi Chake. Pomalizira, pamene Iye anali atapachikidwa pa mtanda, zitachitika kuti moyo uja umene Iye anawukhala sunachite kanthu koma zinthu zabwino, kukhululukira ochimwa, kuchiritsa odwala, ndipo basi kumachita zinthu zimene zinali zabwino. Pamene Iye anali . . . kupuma komaliza pa mtanda, ndi malovu amwano, onyogodola, a iwo amene anaima pambali, akuyenderera pa nkhope Yake yopatulika Iye anafuula, ndi mtima wodzadza ndi chikondi,

“Atate, akhululukireni iwo, pakuti iwo sakudziwa chimene iwo akuchita.”

²³ Iye amatha kumvetsetsa. Pokhala Mulungu, Iye amamvetsetsa. Ndi chifukwa chake Iye anatikonda ife pamene ife tinali osakonedwa, chifukwa Iye ndi Mulungu ndipo Iye amamvetsetsa. “Pokhala moyo, Iye anandikonda ine.” Sipanakhalepo moyo unakhalidwapo wonga umenewo, chifukwa iwo unakulungidwa mu chikondi.

Pakufa, Iye anandipulumutsa ine.

²⁴ Imfa, pamene anali mmunda wa Edeni, Mulungu Yehova anafuna, chilango cha tchimo ndi imfa, ndipo sipakanakhala kusintha. Sizikanasamaliridwa mwanjira ina, iliyonse. Chifukwa, Mulungu ndi wamkulu, ndipo Iye ndi wopanda malire, ndiponso Woweruza wa Miyamba yonse ndi dziko lapansi. Chilango cha tchimo ndi imfa, ndipo panalibe aliyense amene akanamuperekera mzake chilango ichi. Pakuti munthu aliyense, ngakhale iye atamufera munthu mzake, koma iye anali wolakwa kuyamba ndi kuyamba. Panalibepo aliyense wa ife amene akanamuthandiza mzake, chifukwa ife tonse tinali olakwa. “Ife tinabadwira mu tchimo, tinapangidwa mu kusaeruzika, tinabwera mdziko tikuyankhula mabodza.” Ndipo panalibepo chisonyezo cha chiyembekezo, paliponsepo. Ife tinaweruzidwira ku imfa, ndi Mulungu, ndipo cholengedwa chirichonse chimene chinayamba chasunthirapo padziko lapansi chinali pansu pa kutsutsika uku. Pamakhoza kuwuka amuna olungama ndi kumapanga zinthu zazikulu, koma iye amakhala wochimwa kuyamba ndi kuyamba.

²⁵ Panali njira imodzi yokha yoti izo zilipiridwe, ndipo imeneyo inali imfa ya Mulungu Mwiniwake. Chotero Mulungu, pokhala Mzimu, sakanakhoza kufa, koma Iye anadzabwera mu thupi la mnofu ndipo anadzadziwonetsera Yekha mu moyo wa chikondi; kuti adzatenge ubwino wonse umene Iye anali, ndi kudzawupereka iwo mwakufuna ngati Nsembe yapamwamba, kuti Iye adzathe kutenga kulakwa kwa wolakwayo. Tonsefe pokhala ochimwa, ndipo opanda njira mdziko kwa ife kuti tingapulumsidwepo. Iye anabwera osati kuti adzangowonedwa pa dziko lapansi, koma Iye anabwera kuti adzafe ngati Nsembe.

²⁶ Abele anafotokoza izo pamene iye anapereka kwa Mulungu nsembe yapamwamba kwambiri kuposa ya Kaini; pamene iye anamubweretsa mwanawankhosa wamng’ono, atamuzengeza pakhosi pake kachidutswa ka mpesa, kukamumangirira ku mwala. Pamenepo kanagona kanthu kakang’onoko pa mwala, anakokera chibwano chake chaching’ono mmbuyo ndipo, ndi a—a mwala, anakhapa khosi lake laling’onolo; ndipo iko kanaphiriphitha ndi kufa, ndi magazi akuwukha, ndipo ubweya

wake waung'ono woyera unasambitsidwa ndi magari. Abele anawonetsera Kalvare pamenepo.

²⁷ Pamene Mwanawankhosa wa Mulungu, wophedwa kuyambira pa maziko a dziko, anabwera kudzatenga malo a olakwayo, ndipo anasanthidwa ndi kuvulazidwa, ndi—ndi kusereulidwa ndi kusekedwa, ndipo anafa imfa imene palibe cholengedwa chimene chikanafa kupatulapo Mulungu Mwiniwake, ndi tsitsi Lake la magari likulendewera kuchokera mmawo Ake, akudonthera panso, zinawonetsera kuti tchimo ndi chinthu choyipa, pamene Iye anachita kufa kuti adzamuwombole munthu kuchokera ku moyo wa tchimo. Palibe chirichonse chimene chikanafa monga choncho. Palibe chirichonse chimene chikanapirira imfa imeneyo. Amanena kuti, “Pamene iwo anamupyoza mmbali Mwake, kuti, pamenepo panatuluka Magazi ndi madzi.”

²⁸ Inali nthawi ina yapitayo, ine ndimayankhula ndi winawake za izi. Ndipo anali wazasayansi amene anati, “Pali njira imodzi yokha imene zimenezo zikanakhoza kuchitikira. Ndipo si chifukwa cha nthungo ya Chiroma, kuti Iye anafa ndi imeneyo; ndipo sizinalinso chifukwa chotaya Magazi, kuti nchifukwa Iye anafa, chifukwa Magazi anali alipobe mu thupi Lake. Chimene Iye anafa nacho, sichinali chifukwa cha nthungo ya Chiroma kapena misomali imene inakhomeredwa mmanja Mwake, kapena chisoti chaminga chimene iwo anachiika pamutu Pake. Koma chifukwa... Iye anafa ndi chisoni, chifukwa Iye anadza kwa Ake Omwe ndipo Ake Omwe sanamulandire Iye ayi. Iye anafa chifukwa chosweka mtima. Pamene, Iye ankadziwa zolengedwa kumene za nthawi, zimene Iye akanadzafa kuti aziwombole, zinamulavulira pa nkhope Yake, ndipo Iye anakanidwa ndi munthu.”

²⁹ Davide, zaka eyiti handiredi izo zisanachitike, analira ndi liwu lomwe lija limene Iye analira pa Kalvare, “Mulungu Wanga, nchifukwa chiyani Inu mwandisiya Ine?”

³⁰ Ndi chinthu chowopsya bwanji chimene tchimo limachita, ilo limamulekanitsa munthu kwa Mulungu! Ndipo Iye anali nsembe ya tchimo imene inkayenera kuti iperekedwe kwa machimo athu. Ndipo Iye analekanitsidwa kuchoka pa Kukhalapo kwa Mulungu. Tchimo linali litamulekanitsa Iye. Mulungu anadzaika machimo athu pa Iye, ndipo Iye analekanitsidwa kwa Mulungu, ndipo ndi chifukwa chake Iye anafuula, “Nchifukwa chiyani Inu mwandisiya Ine?” Ndipo chifukwa chakuti Iye anasiyidwa, ndipo anali atatenga malo awa, ndipo nkumawawona anthu Ake, amene Iye anabwera kuti adzakhale Mpulumutsi wawo ndi kuti adzawapatse iwo Moyo, iwo anali atamukana Iye, ndipo izo zinamukhumudwitsa Iye, kwambiri, mpaka kuti Iye anasweka mtima kwambiri mpaka Magazi ndi madzi, ndi zamadzi za mthupi Lake, zinalekana.

³¹ Munthu sazadziwa konse chimene icho chinali. Ndi chifukwa chake sipakanakhala wina aliyense amene akanafa monga choncho. Ine sindikusamala kuti inu mungazunzidwe mochuluka bwanji, mmene iwo angaikire mapazi anu mu zitsa, kapena kukudulani inu, nthulinthuli, kapena kukuwotchani inu nthulinthuli; inu simungafe imfa imeneyo, chifukwa mapangidwe anu si wonga chomwecho. Iye ankayenera kukhala Mulungu. Iye ankayenera kukhala, woposa munthu. Ndipo kuganiza, kuti, Mulungu anafa. Iye anafa chifukwa chosweka mtima, ndi chisoni choterocho chifukwa cha dziko, mpaka zamadzi za mthupi Mwake zinachitika mwa mtundu wina zimene sizingachitike mwa inu. Inu simungathe kuzunzika monga chomwecho. Palibepo njira imene inu mungakhale ndi chisoni cha mtundu umenewo. Chotero alipo Mmodzi yekha amene angathe kuchita zimenezo, ndipo Iye anachita izo.

³² Pamenepo utapachikika, moyo wofunika uja umene sunkadziwa kanthu koma chikondi ndi kuchita zabwino, unapachikika pamenepo pakati pa Miyamba ndi dziko lapansi, anakwezedwa mmwamba pamenepo, anavulidwa maliseche, anachititsidwa manyazi. Taganizani mmene inu mukanakhalira, kuvulidwa maliseche; inu simungadziwe kuchititsidwa manyazi kuposa mmene Mulungu angachitire, atapachikidwa pamenepo. Ine ndikudziwa mtanda uli ndi kanthu kakang'ono, ngati kuti iwo anaika chinachake momuphimba Iye, koma iwo sanachite konse zimenezo. Izo zinangoikidwa pa mtanda, kapena wojambulayo anaika izo pamenepo. Iwo anamuvula Iye zovala Zake. Iye anali atavala mwinjiro, ndipo iwo anamung'ambira Iye ndipo anapangira maere. Iye anachititsidwa manyazi, motheratu. Komabe, pokhala Mulungu, ankayenera kupirira nazo, ndipo ochimwa anamulavulira mate pa nkhope Yake. Komabe, pokhala kuti anali—kuya kumene kwa khalidwe, ankayenera kuti afe pagulu, ndikuvulidwa maliseche. Zinamukhudza kwambiri Iyeyo, mpaka izo zinalekanitsa madzi ndi Magazi. Nzosadabwitsa... Ine ndikuganiza wandakatulo anafotokoza bwino izo pamene iye anati:

Pakati pa miyala yosweka ndi mlengalenga
mwamdima,
Mpulumutsi wanga anaweramitsa mutu Wake
ndipo anafa;
Koma chotchinga chotseguka chinaulula njira
Ya kuchisangalalo cha Kumwamba ndi tsiku
losatha.

³³ Ndithudi, Iye ankayenera kuti achite zimenezo. Chotchingacho chinapachikidwa pakati pa munthu ndi Mulungu, ndipo chotchingacho chitatseguka chinawulula njira yopita ku chisangalalo cha Kumwamba ndi tsiku losatha. Kalvare amatanthauza chinachake, amatanthauza zochuluka kuposa zimene ife tingazifotokoze. Ndithudi.

Pokhala moyo, Iye anandikonda ine. Pakufa,
Iye anandipulumutsa ine.
Poikidwa mmanda, Iye anatengera machimo
anga kutali.

³⁴ Ilo laweruzidwa tsopano. Tchimo liribenso pogwira. Pamene Iye anafuula pa mtanda, “Kwatha,” tchimo linafa! Tsopano ilo ndi lakufa. Ilo anathana nalo. Ilo ndi lopanda mphamvu. Ilo liribe moyo. Taganizani za izo, anthunu. Tchimo limenero, mdani kwa anthu, ndi lakufa ndipo liribe moyo, ilo liribenso chochita. Ilo silingathe. Nzosadabwitsa dzuwa linatseka kupenya kwake, nyenyezi zinalephera kuti ziwale, dziko linada mdima, ilo lonse linali likuwomboledwa.

³⁵ Tsopano ilo ndi lakufa, ilo linaikidwa mmanda, ilo liribe moyo. Ilo liribe moyo mkati mwake, ndiye ilo likuyenera kuikidwa mmanda. Chinaikidwa mmanda ndi chiyani? Thupi la Mulungu linaikidwa mmanda, pakuti ilo linali nsembe ya tchimo. Ilo linali Mwanawankhosa wopyereza, ilo linapyeredwa ndi moto wa kusaeruzika. Mwanawankhosa wopanda tchimo uja amene sankalidziwa nkomwe tchimo, Mulungu uja Yemwe sankadziwa cholakwika; moyo Wake unali utaperekedwa, ndipo pamenepo panapachikidwa nsembe ya tchimo. “Poikidwa mmanda, Iye anatengera machimo anga kutali.” Iye ankayenera kuikidwa mmanda. Thupilo, nsembe ya tchimo inkayenera kuikidwa mmanda.

³⁶ Ndi chifukwa chake ambiri, posakhalitsapa, akhala akuyenda, mmodzi ndi mmodzi, kubwera ku dziwe ili, kuti adzabatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu. Bwanji? Chinachake chachitika. Mzimu uja umene unatuluka kuchokera mu thupi limenelo, pamene Iye anafuula, “Kwatha,” waliweruza tchimo mmatupi athu. Ndipo ife tikuyenera kukaliika ilo mmanda, kuti lisadzakumbukiridwensho. Ndine wokondwa kuti ilo latero.

³⁷ Pamene chirichonse chikwiriridwa, icho chimabisika, icho sichimawonekansho. “Ndipo poikidwa mmanda, Iye anatengera machimo anga kutali.” Mulungu sawonansho machimo athu panonso, pakuti iwo anakwiriridwa. Anakwiriridwa kuti? Mu Nyanja ya Kuiwala. Taganizani za Nyanja ya Kuiwala! Mulungu sangawakumbukirenso iwo, chifukwa iwo anachitidwa ziwiri zonse anafa ndipo anakwiriridwa mmanda. Iwo sangakumbukiridwensho. Iwo anachoka mu kukumbukira kwa Mulungu.

³⁸ Iye analinso a . . . mu “kuikidwa” uku Iye anaimiriridwa mu Chipangano Chakale. Iwo amakhala ndi ziwiri . . . Iwo amakhala ndi nsembe ya tchimo pa kuyeretsewa kwa kachisi. Ndipo nsembe ya tchimo imeneyo imakhala yakuti iwo amatenga mbuzi ziwiri, ndipo mbuzi imodzi imaphedwa; ndipo mbuzi inayo, imakhala ndi machimo amene anali pa mbuzi yakufayo amakaikidwa pa mbuzi yamoyoyo.

³⁹ Kumbukirani, Yesu anali Nkhosa. Iye anali Mwanawankhosa, koma mu nkhani iyi Iye anadzakhala mbuzi. Iye anali chirungamo chifukwa Iye anali Mulungu, Nkhosa. Koma Iye anadzakhala mbuzi, tchimo, kuti Iye adzathe kukhala nsembe ya tchimo kwa ine ndi inu; kuchokera ku Nkhosa anadzakhala mbuzi.

⁴⁰ Ndipo Yesu anaimiriridwa mu nyama ziwiri zonsezo, mbuzi ziwiri zonsezo: Kwa imodzi, iye anafera—iye anafera chitetezero; yachiwiriyo, machimo amene anali pa chitetezerocho anadzaikidwa pa azazeli, ndipo azazeli anatenga machimo a anthu ndipo anapita kutali ku chipululu, kuti akasenze machimo a anthu. Kodi icho chinali chiyani? Icho chinali imfa ndi kuikidwa mmanda kwa Ambuye Yesu athu. “Pakufa. . . Pokhala moyo, Iye anandikonda ine. Pakufa, Iye anandipulumutsa ine. Poikidwa mmanda, Iye anatengera machimo anga kutali.” Iye anadzitengera machimo a anthu pa Iyemwini, ndipo anawanyamulira iwo kukalowa nawo mu hade wotsikitsitsa. Iye anali nsembe ya tchimo. Iye anali ndi machimo a anthu. Iye anawafera iwo. Ndiponso machimo anaikidwa pa Iye, ndipo Iye anatengera machimo athu kutali, kutali kwambiri mpaka Mulungu sangathe kuwawonanso iwo. Taganizani za zimenezo! Oh, Mpingo ukhoza kufuula, “Aleluya chifukwa cha Mpulumutsi woteroyo!”

⁴¹ Sikuti machimo athu anangokhululukidwa kokha, koma iwo akakwiriridwa mu Nyanja ya Kuiwala, kuti asadzakumbukiridwensho. “Poikidwa mmanda, Iye anatengera machimo athu kutali.” Iwo sangakumbukiridwensho, pakuti iwo anapita. Iwo anachoka mmaso a Mulungu. Iwo anapuwalitsidwa. Iwo anasudzulidwa. Iwo anakaikidwa kutali. Mulungu samawakumbukiranso iwo. Chiyani? Mpingo ukuyenera kusangalala mmawa uno, podziwa kuti machimo athu sadzakumbukiridwanso. Iwo anakaikidwa mu Nyanja ya Kuiwala, anapita kumanda koti sikungakhaleko chiukitsiro chirichonse. Iwo anafa kwanthawizonse, ndipo anaiwalidwa. Iwo ali ngati iwo sanachitike nkomwe. “Pakufa, Iye anandipulumutsa ine.” Koma, “Poikidwa mmanda, Iye anatengera machimo anga kutali.” Iye anawatengera iwo kutali mpaka iwo anakalowa mu Nyanja ya Kuiwala. Oh! Ife tikudziwa kuti zinthu zimenezo zimakhulupiridwa ndithudi pakati pathu, ndipo izo ndithudi ndi Choonadi. Izo ndi Choonadi cha Mulungu. Zinthu zazikulu zonsezo zinali zosati kuti munthu angazifotokoze. Ife sitingathe nkomwe kufotokoza kuthokoza kwathu kwa zinthu zoterozo.

⁴² Koma, oh, Isitara imeneyo! “Powuka, Iye analungamitsa mwaulele kwanthawizonse.”

Pokhala moyo, Iye anandikonda ine. Pakufa,
Iye anandipulumutsa ine.

Poikidwa mmanda, Iye ananyamulira machimo
 anga kutali. (Izo zinali zabwino.)
 Koma, powuka, Iye anandilungamitsa.

⁴³ Kuuka kumeneko kunali chiyani? Linali lisiti la Mulungu, kuti mtengo walipiridwa. “Powuka, Iye anandilungamitsa mwaulele kwanthawizonse.” Oh, ndi Mpulumutsi bwanji, kuwuka! Kodi Mulungu anachita chiyani? Munthu akhoza kuzunzika, munthu akhoza kufa, munthu akhoza kuikidwa mmanda. Koma Isitara inali chachikulu kwambiri cha zonsezo, pakuti kunali kuvomereza kwa Mulungu, “Malamulo anga akwaniritsidwa, zofuna Zanga zakwaniritsidwa, ndi Iyeyo!” Iye anamuukitsa Iye kwa akufa! “Powuka, Iye anandilungamitsa mwaulele kwanthawizonse.” Lodala likhale Dzina Lake Loyera!

⁴⁴ Nzosadabwitsa izo zimabweretsa kutengeka! Nzosadabwitsa mtima wa munthu sungathe kuzigwira izi! Oh, ndi chikhulupiriro chathu chogonjetsa ife tikhoza kuima kutsidya ndikuti, “Ife talungamitsidwa kwanthawizonse, mwaulele,” chifukwa Iye anafa ndipo anaikidwa mmanda, ndipo Mulungu anamuukitsa Iye kenanso mmawa wa Isitara. Kenako, Mulungu anadzawonetsera kuti Izo zalandiridwa, zinthu zonse zimene Iye anazichita. Chirichonse chinaperekedwa mwaulele, inu mukhoza kupita amfulu tsopano! “Powuka, Iye anandilungamitsa mwaulele kwanthawizonse.” Oh, palibe amene angadziwe nkomwe, sangathe kuganzira za tsiku lalikulu ilo pamene Iye anauka! Ndipo Angelo anaziwona izo. Mmiyamba ya mmiyamba, Angelo anaimba matamando a Mulungu, ndipo anasangalala; pamene oyera a Chipangano Chakale, mu Paradiso, anafuula, “Aleluya!” “Powuka, Iye anandilungamitsa.” Miyamba inagwedezeka, dziko linagwedezeka, paradiso anagwedezeka, ndipo Kumwamba kunagwedezeka, pamene Liwu lalikulu lija linatulukira. Kudzuka kuchokera mmanda Iye anauka! “Powuka, Iye anandilungamitsa mwaulele kwanthawizonse.” Oh, mai!

⁴⁵ Ndiye oyera amene amafa mwa iye akhoza kuimba iyi, pamene ife tiyang’ana pa chisomo chodabwitsa icho, kumeneko, zimene Iye anachita. Mukuona? Chivomerezo chosindikizidwa cha Mulungu! “Kanthawi pang’ono ndipo dziko silindiwonanso Ine, komabe inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine ndidzawuka kwa akufa ndipo ndizidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumathelo a dziko; ngati chotsimikizira, ndiponso kutsimikizira kuti zimene Mulungu ananena ndi zoon, ndi zimene ine ndikunena ndi zoon,” Yesu anati. “Ine ndidzabwera mu mawonekedwe a Mzimu Woyera. Ine ndidzapanga pokhala Panga ndi inu, ndipo ndidzakhala ndi inu kwanthawizonse.” Ndiye oyera amene ali ndi chiyebekezo cha chikhulupiriro chimenecho mu mtima mwawo, akhoza kuimba nyimbo iyi.

Mmawa wowala wopanda mitambo pamene
 akufa mwa Khristu adzawuka,
 Ndi kugawana ulemerero wa chiwukitsiro
 Chake;
 Pamene osankhidwa Ake adzasonkhana
 kupita kwawo kuseri kwa mlengalenga, (ndi
 chilimbikitso changwiwo, ndi Chisindikizo
 cha Mulungu, ndi lisiti lolembedwa
 lochokera kwa Mulungu Mwiniwake)
 Akamadzaitana dzina langa, ine ndidzakhala
 komweko. (Oh, bwerani msanga!)

Oh, nzosadabwitsa iwo anati:

Pokhala moyo, Iye anandikonda ine. Pakufa,
 Iye anandipulumutsa ine.
 Poikidwa mmanda, Iye anatengera machimo
 anga kutali. Oh!
 Powuka, Iye analungamitsa mwaulele
 kwanthawizonse.

⁴⁶ Machimo akhululukidwa. Nsembe zonse izi bwenzi
 ziri nthano, nsembe zonsezi zikanakhoza kulephera. Koma
 pa mmawa wa Isitara, pamene Iye anadzauka, Mulungu
 anatsimikizira kuti Iye wavomereza Izo. Nzosadabwitsa,
 izo zimaubweretsa mtima wa munthu ku aleluya!
 Nzosadabwitsa izo zimapangitsa amuna kuima pamaso pa
 imfa! Zimawapangitsa anthu kutchula zinthu izo zimene
 panalibepo, ngati kuti izo ziripo! Koma bwanji? “Powuka, Iye
 anandilungamitsa.” Inu mukudziwa bwanji kuti iye wauka?
 Chifukwa, Iye wauka mmitima mwathu, talungamitsidwa
 mwaulele kwanthawizonse!

⁴⁷ Masiku forte kenako, pamene Iye anaima, akuyankhula
 kwa ana Ake, mphamvu yokokera pansu inayamba kulephera
 kugwira. Ntchito zinali zitatha. Mtengo unali utalipiridwa.
 Iye anali ali ndi lisiti mdzanja Lake. Ilo linali lisiti la
 Mulungu. Iye anali ndi ana, Mpingo, okhulupirira. Tchimo lonse
 linali litagonjetsedwa. Njira inali itayeretsedwa. Iye sibwenzi
 atakhalanso padziko lapansi. Nchiyani chimatigwirira ife kuno?
 Mphamvu yokokera pansu. Mphamvu yokokera pansu inayamba
 kusweka, iyo inataya kugwira kwake. Bwanji? Zonse zinali
 zitatha pamenepo. Chinachitika ndi chiyani? Iye anayamba
 kukwera kuchokera pa dziko lapansi.

⁴⁸ “Pitani inu mu dziko lonse, ndipo mukalalikire Uthenga
 kwa cholengedwa chirichonse,” panadzabwera kuyankhula kwa
 milomo Yake. “Pitani inu mu dziko lonse, ndipo mukalalikire
 Uthenga kwa cholengedwa chirichonse. Iye amene akhulupirira
 ndipo nabatizidwa adzapulumutsidwa, iye amene sakhulupirira
 adzawonongedwa. Ndipo zizindikiro izi zidzawatsata iwo
 amene akhulupirira. Mu Dzina Langa iwo adzathamangitsa

mizimu yoipa. Iwo adzayankhula ndi malirime atsopano. Ngati iwo adzatola njoka kapena kumwa zinthu zokupha, izo sizidzawapweteka iwo. Ngati iwo adzaika manja awo pa odwala, iwo adzachira. Chifukwa ine ndiri moyo... Mphamvu yokokera pansi yasweka pa Ine. Tchimo linasowa pogwira. Ine ndinakuferani inu. Mulungu anatsimikizira izo, ndipo anapereka lisiti la chiukitsiro. Ndipo chifukwa choti Ine ndiri moyo, inu mudzakhalanso moyo! Tsiku lina Ine ndidzabwereranso.”

⁴⁹ Tsiku lina Iye akubwera, oh, tsiku la ulemelero! Ndiye, mmodzi... Pokhala moyo, pakufa, poikidwa mmanda, pakuwuka, akubweranso, chiyembekezo cha Mpingo lero!

Pokhala moyo, Iye anandikonda ine. Pakufa,
Iye anandipulumutsa ine.
Poikidwa mmanda, Iye anatengera machimo
anga kutali.
Powuka, Iye analungamitsa mwaulele
kwanthawizonse.
Tsiku lina Iye akubwera, oh, tsiku
laulemerero!

Icho chinali chiyani? Zinthu faifi mu zilembo faifi, J-e-s-u-s.

Pokhala moyo, Iye anandikonda ine. Pakufa,
Iye anandipulumutsa ine.
Poikidwa mmanda, Iye anatengera machimo
anga kutali.
Powuka, Iye analungamitsa mwaulele
kwanthawizonse.
Tsiku lina Iye akubwera, oh, tsiku
laulemerero!

⁵⁰ Ife tikuyembekezera Kudza Kwake Kwachiwiri!

Ndipo ena a mmawa owala ndi opanda
mitambo awa
Pamene akufa mwa Khristu adzawuka,
Ndi kudzagawana ulemmerero wa chiwukitsiro
uwo;
Pamene osankhidwa Ake adzasonkhana
kwawo kuseri kwa thambo,
Pakuitana dzina langa, ndidzakhala komweko.

Bwanji? Ine ndiri ndi lisiti. Iye anauka! Inu mukudziwa bwanji? Iye akukhala moyo mu mtima mwanga. Iye akukhala moyo mu mtima wa mpingo Wake wokhulupirira.

⁵¹ Taganizani za zimenezo, amzanga. Dziwe likhala litakonedwa mu mphindi pang'ono chabe, ndi madzi otentha, kwa utumiki wa ubatizo, mwamsanga ife tikamabwerera.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu kwa mphindi chabe.

⁵² Ine ndikudabwa lero, ngati pangakhale mmodzi pakati pathu, kapena ambiri amene sanamvetsetsebe Nsembe iyi mokwanira kuti angaivomereze Iyo, ndipo inu mukufuna kuti mukumbukiridwe mu pemphero, kuti Mulungu ayankhule mwachirendo mu mtima mwanu, kuti inu muvomereze Nsembe Yake, kuyeretsa kwa solo yanu.

⁵³ Ndipo mukumbukire kuti lero ife sitikungosangalalira nthawi yoti tivale zipewa zatsopano ndi kuvala zovala zatsopano; chimene ndi chabwino, icho ndi chizindikiro cha chinachake chatsopano. Mulungu anapanga chinachake chatsopano. Chimene, ndi chabwino. Izo si zokhazo. Isitara siimatanthauza zimenezo. Kapena, kukasaka akalulu a Isitara kapena mazila a kalulu, ndi nkuku zazing'ono zoyera, ndi zina zotero, lingaliro lake si limenelo, m'bale.

⁵⁴ Isitara ndi kugonjetsa, ndi chigonjetso chimene Mulungu anachipereka pa dziko lapansi, kuti Iye anawukitsa Mwana Wake Yemwe kwa akufa. "Kuti aliyense amene akhulupirira mwa Iye, asadzawonongedwe, koma adzakhale nawo Moyo Wamuyaya."

⁵⁵ Chiukitsiro chikhoza kukhala mu moyo wanu momwe. Ngati inu mulibe icho, kodi mungakweze dzanja lanu kwa Iye mmawa uno, pamene inu mwaweramitsa mitu yanu, ponena kuti ndi ili, "Mulungu, mundikumbukire ine, kuti Moyo wa chiukitsiro uwo, mulole Iwo ukhale mu mtima mwanga." Inu mungakweze dzanja lanu ndikuti, "Mundipempherere ine, M'bale Branham, pamene ine ndikukweza dzanja langa"? Ambuye akudalitseni inu. Ambuye akudalitseni inu. Kodi alipo wina amene mungakweze dzanja lanu, ndikuti, "Mundipempherere ine, m'bale, ine ndikufuna kuti ndilandire Moyo wachiukitsiro uwu"?

Mmawa wowala ndi wopanda mitambo,
(taganizirani izo tsopano pamene
ife...?....)... Khristu adzawuka,

Kudzagawa ulemerero wa chiwukitsiro Chake;
Pamene osankhidwawo adzasonkhana ku
gombe,

Pakuitana dzina langa, ndidzakhala komweko.

Pakuitana dzina langa,

Pakuitana dzina langa,

(Tsopano ngati inu simukutsimikiza, mukonze
izo, tsopano)... adzaitana dzina langa,
Pakuitana dzina langa, ndidzakhala komweko.

Tiyeni timutumikire Ambuye kuyambira...

(Ichi ndi cha inu oyera)... dzuwa,

Tiyeni tiyankhule...

⁵⁶ Tsopano, inu amene muli Akhristu, mukufuna kulumbirira kwa Mulungu, kuti mukagwira ntchito mochuluka; bwerani kuno, kwezerani dzanja lanu kwa Iye.

Ndipo pakuitana dzina langa, ndidzakhala komweko. (Ambuye akudalitseni inu.)

Pakuitana dzina langa,
Pakuitana dzina langa,
Pakuitana dzina langa,
Pakuitana dzina langa, ndidzakhala komweko.

⁵⁷ Wokonededwa Mulungu, Inu mwaona mtima uliwonse muno, ndipo Inu mukudziwa zolinga ndi zofuna. Ndipo ine ndikupempha chifundo. Mulungu, mupereke izi, kuti chifundo chiwonetseredwe kwa anthu awa. Iwo abwera mmawa uno chifukwa cha ora ili la kudzapembedza. Iwo abwera pa—pa malo ano kuti adzamve Mawu Anu.

⁵⁸ Ndipo monga ife timayankhulira, kuti, pamene Inu munkhala moyo, sipanakhalepo moyo ngati Wanu. Pakufa, Inu munali Mmodzi yekhayo Amene akanafa mwanjira imeneyo. Pamene Inu munaikidwa mmanda, Inu munanyamulira machimo athu kutali; mutazitengera machimo a anthu pa Inu, Inu munawatengera iwo ku Nyanja ya Kwiwala. Koma, powuka, Inu munalungamitsa mwaulele kwanthawizonse. Ndipo ife tikuima, lero, kuyembekezera Kudza Kwanu.

⁵⁹ Mulungu, adalitseni iwo. Tithandizeni ife. Ife tikuzindikira kuti ife tiribe nthawi yochuluka, pakuti izo zangokhala pakhomo. Ndipo iliyonse. . . Ndipo ora limodzi kuchokera pano, mogwirizana ndi azasayansi, mafuko akhoza kusakhalaponso. Ndipo ife tikupemphera, Mulungu, pamene ife taima, mmawa wa Isitara uno pa chiundo cha Kudza Kwake, chiyembekezo cha Mpingo. Masauzande ambiri akugona uko mu fumbi la dziko lapansi, akudikirira ora limenelo, miyoyo yawo ili pansu pa guwa, ikufuula, “Mpaka liti, Ambuye? Mpaka liti?” Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu muyankhule ndi ife. Ndipo mutilole ife tikumbukire kuti ziribe kanthu zimene ife tingapange kuno kudziko lapansi, izo ndi zazing’ono kwambiri. Ndipo chinthu chokhacho chimene ife tingachite tsopano, ndi kudikirira Kudza Kwanu, ndi kukamuuza aliyense. Uthengawu ndi wamsanga. Mulole ife tiwutengere iwo kwa anthu, mwamsanga, kuti Inu mukhoza kubwera nthawi iliyonse. Asanafike mabomba awa amene ife tikuwakamba, ndi mizinga iyi, imene ikhoza kukhala mivumbi ya masauzande a iyo akugwera padziko lapansi mu nthawi ya miniti imodzi; zimenezo zisanachitike, Inu mwalonjeza kuti mubwera, Ambuye, kudzatenga anthu Anu. Izo zidzakhala mwanjira imeneyo, Ambuye. Chotero, pafupifupi miniti iliyonse, pakhoza kukhala chiukitsiro, Isitara kwa Mpingo; chiukitsiro kuchokera ku moyo wa tchimo uwu, kupita ku Moyo Wamuyaya, kudzera mwa Khristu. Imvani mapemphero athu.

⁶⁰ Ndipo lero, pamene ife tikupita ku mautumiki enawo, kupita mu kuphunzitsa kwa Sande sukulu, O Ambuye, yankhulaninso,

ndipo mulole mitima yambiri ichenjezedwe mwachirendo. Ndipo mulole iwo abwere mu madazeni, kubwera mu dziwe ili mmawa uno, mmawa wa Isitara uno, kuti adzaikidwe mmanda ndi Ambuye Yesu, kuvomereza Nsembe Yake. Ziribe kanthu kuti iwo ndi a mpingo wanji, kapena ndi gulu lanji la chipembedzo limene iwo amayanjana nalo, zimenezo sizitanthauza kanthu. Koma kodi iwo aivomereza Nsembeyo? Kodi iwo akuvomereza kuti iwo si abwino, kuti Yesu anali Yekhayo amene anali wabwino? Ndipo Iye anatifera ife, mmalo mwathu. Ndipo Iye anatenga machimo athu ndipo anakawakwirira iwo, ndipo ife tikuima tokha mwa Iye. Mipingo yathu siingathe kukwirira machimo athu, moyo wathu womwe sungathe kukwirira machimo athu, koma Khristu anakwirira machimo athu mu Nyanja ya Kuiwala. Mulungu, perekani tsopano kuti zinthu izi zikakhale za ulemelero pamaso Panu.

⁶¹ Ndiye usikuuno, Ambuye, mubwere mu mphanvu ya chiukitsiro Chanu, ndipo mudzagwedeze malo aang’ono awa ngati kuti iwo sanayambe agwedezekapo. Mulole zizindikiro ndi zodabwitsa ziwonekere. Mubwereze izi, monga zinachitikira ma Lamlungu angapo apitawo, Ambuye, pamene odwala ndi osautsika anachiritsidwa mopambana. Ife tikupemphera kuti izo zichitikenso usikuuno, kwa ulemelero Wanu, Ambuye.

⁶² Mutikhululukire ife mphulupulu zathu tsopano, Ambuye, ndipo mulole iyi, ikhale Isitara yeniyeni kwa ena a ife, Isitara yeniyeni kwa tonse a ife. Ndipo ena a iwo amene sanayambe adziwapo chimene mdalitso wa Isitara uli, mulole likhale lero limene Khristu ati awuke mu mtima mwawo, ndi chiyembekezo chatsopano, ndi Moyo watsopano. Alozeleni iwo ku Kalvare. Pakuti ife tikupempha izi, mu Dzina la Yesu. Amen.

⁶³ [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi]...tikhale ndi nthawi iyi ya chiyanjano. Ndi angati a inu mumawakonda Ambuye? Ingokwezani mmwamba dzanja lanu. Oh, mai, izo ndi zopambana!

⁶⁴ Ine ndamva kuti inu muli ndi mwana woti adalitsidwe, M’bale McDowell. Inu mubweranso ku msonkhano wa Sande sukulu, inu mutero? Chabwino, izo zikhala zabwino. Pamenepo ndi pamene ife titi tidalitse ana ndi zina zotero, nthawi imeneyo, ngati inu simudandaula, izo ziri bwino.

⁶⁵ Ndipo chotero tsopano, ife tibalalitsa omvetsera kwa mphindi pang’ono, kuti inu mupite ku malo anu ndipo mukadye kadzutsa, kenako mubwererensho. Ndife okondwa kuti inu munali pano.

⁶⁶ Ndipo tsopano, tiyeni tingoima. Ndipo nyimbo yomwe ija imene ife timaimba mphindi zapitazo, “Pa lowala ndi lopanda mitambo lija...” Ndi angati amene ali ndi chiyembekezo chimenecho mwa iwo? Tiyeni tikuwoneni mukukweza dzanja lanu. Imirirani.

...lowala ndi lopanda mitambo (Imbani iyo tsopano.)

...pamene akufa mwa Khristu adzawuka,
Ndi kugawana ulemerero wa chiwukitsiro
Chake;

Pomwe opulumutsidwa a mdziko
adzasonkhana mbali inayo,
Ndipo pakuitana dzina langa, ndidzakhala
komweko.

Pakuitana dzina langa,
Pakuitana dzina langa,
Pakuitana dzina langa,
Pakuitana dzina langa, ndidzakhala komweko.

⁶⁷ Tsopano, pamene tikuimba ndime yotsatirayo: “Tiyeni timutumikire Ambuye, kuyambira mmawa mpaka kulowa kwa dzuwa, tiyeni tiziyankhula,” (osati za zinthu za mdziko) “koma, tiyeni tiziyankhula za zodabwitsa Zake zonse, chikondi ndi chisamaliro.”

Pamene ife tikuchita izi, tizigwirana dzanja ndi winawake kumbuyo kwanu, kutsogolo kwanu, mmbali mwanu. Tiyeni tonse tichite zimenezo tsopano. Ndikuti, “Mmawa wabwino, mzanga Wachikhristu, ndine wokondwa kukhala mu tchalitchi ndi iwe.” Chabwino.

Tiwatumikire Ambuye kuyambira . . .
...za chikondi Chake chodabwitsa ndi
chisamaliro;
Pomwe moyo ukadzatha, ndipo ntchito
zathanso,
Ndipo pakuitana, ndidzakhala komweko.
Pakuitana dzina langa,
Pakuitana dzina . . .
. . . dzina langa,
Pakuitana dzina langa, ndidzakhala komweko.

Bwanji? Ife tidzakakhalako chotani kumeneko? Chifukwa: “Pokhala moyo, Iye anandikonda ine. Pakufa, Iye anandipulumutsa ine. Poikidwa mmanda, Iye anatengera machimo anga kutali. Powuka, Iye analungamitsa mwaulele kwanthawizonse. Tsiku lina Iye akubwera, oh, tsiku la ulemerero.”

Pakuitana dzina langa, ndidzakhala komweko.
(Ife tiri ndi lisiti.)

. . . pakuitana . . . dzina,
Pakuitana dzina langa,
Pakuitana dzina langa,
Pakuitana dzina langa, ndidzakhala komweko.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu.


⁶⁸ Ambuye, mmawa wina wowala ndi wopanda mitambo, pamene ife tidzawona utawaleza waukulu uwo ukubwera mu mlengalenga (Chizindikiro cha Mulungu cha pangano, pangano losatha: Iye wasunga lonjezo Lake.), ndiye ife tidzayang'ana, akubwera, ndipo mitumbira ya kumanda idzakhala ikutseguka, ndipo iwo amene anagona mu fumbi la dziko lapansi adzauka kuti akagawane naye Iye ulemelero wa Isitara yoyamba, Amene anapanga izo kukhala zotheke, Ambuye wathu. Zikomo Inu chifukwa cha zimenezo, Ambuye. Ndine wokondwa kwambiri, Ambuye, kuti chiyembekezo chiri pachifuwa changa. Pakuti ine ndikuwona mapewa anga akugwa, Ambuye, ndipo—ndipo ukalamba ukuyamba kukwawiramamo; ine ndiri pamwamba pa phiri, ndikuyang'ana uko tsopano. Ambuye, ndine wokondwa kwambiri kuti chiyembekezo chimenecho chikuyaka mkati mwanga. Tsiku lina Inu mudzabwera. Ndine wokondwa kwambiri kuti pali ambiri pano lero amene akumverera chimodzimodzi.

⁶⁹ Ine ndikupemphera, Ambuye, kuti Inu mutipatse ife tsiku lopambana, lero, kutikhululukira mphulupulu zathu zonse, pamene ife tikuvomereza kulakwa kwathu, ndi kuvomereza kuti ife si oyenera. Koma imfa ya Khristu, kuikidwa mmanda, chiukitsiro, zinatsimikizira kwa ife mwa Mzimu Wake umene waukitsidwa mmitima mwathu, kutipanga ife kukhala gawo la chiukitsiro Chake, ndipo ife tiri ndi chikole cha chiukitsiro chathu mmitima yathu tsopano. Chifukwa kwa tchimo, ife tafa, ndipo ife talowa mu Moyo watsopano, ndipo tauka kwa zinthu zakale za mdziko tapita ku Moyo watsopano. Icho ndi chikole, dipo, O Ambuye, icho—icho ndi chikole cha chiukitsiro chathu.

⁷⁰ Ndife okondwa kwambiri kumverera izo ndi kusangalala izo pa wina ndi mzake. Zinthu izi, ife timazigwira ngati chuma chopambana cha mitima yathu, chinachake chimene palibe ndalana ingagule, dziko silingathe kuzifufuta, chifukwa Mulungu anazipereka izo kwa ife mwaulele, ulele monga Khristu anafera izo.

⁷¹ Tsopano, ife tikupemphera kuti Inu mukhale nafe mmawa uno. Mutithandize ife, tsopano, ndipo kuti tikapumulire mphindi pang'ono, ndipo tidzabwererenso. Mutipatse ife msonkhano wotsatira wopambana. Pakuti ife tikupempha izi, mu Dzina la Iye, Amene anatiphunzitsa ife kuti tizipemphera limodzi [M'bale Branham ndi osonkhana akupemphera limodzi—Mkonzi]: Atate athu Amene muli Kumwamba, Dzina Lanu Lilemekezedwe. Ufumu Wanu udze. Kufuna kwanu kuchitidwe padziko lapansi, monga izo ziriri Kumwamba. Tipatseni ife lero chakudya chathu cha lero. Ndipo mutikhululukire ife zolakwitsa zathu, monga ife tiwakhululukira iwo amene atilakwira ife. Ndipo musatitsogolere ife mu mayesero, koma mutipulumutse ife kwa

zoipa: Pakuti Wanu ndi Ufumu, ndi mphamvu, ndi ulemerero, kwanthawizonse. Amen.

⁷² Ambuye akudalitseni inu, tsopano, mpaka ife tidzakuwoneni inu, mu pafupifupi a . . . pa hafu-naini. Inu mugwirane chanza wina ndi mzake; ndipo ife tikuonani inu pa hafu-naini. 

KUKHALA MOYO, KUFA,
KUIKIDWA MMANDA, KUWUKA, AKUBWERA CHA59-0329s
(Living, Dying, Buried, Rising, Coming)
MAULALIKI A ISITARA

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, unalalikidwa mu Chingerezi pa Isitara Lamlungu mmawa pa kutuluka kwa dzuwa, Marichi 29, 1959, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2020 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org